

# العَقِيْدَة لِلْأَطْفَال

# ‘Aqīdah kwa Ana

**Mlembi**:

Abū Hashmah Al-Malāwī

**Editor**: Uthmān Chikapa

**Buku 1**

# مَعْرِفَةُ اللّٰهِ

## KUMUDZIWA ALLĀH

| | |
|---|---|
| Kodi Allāh ndi ndani? | مَنْ هُوَ اللّٰهُ؟ |
| Allāh ndi Mbuye wanga | اللّٰهُ رَبِّي. |
| Allāh adandilenga ndipo amandiongolera. | اللّٰهُ خَلَقَنِي وَهُوَ يَهْدِينِ. |
| Iye amandidyetsa komanso kundimwetsa. | وَهُوَ يُطْعِمُنِي وَيَسْقِينِ. |
| Ndikadwala, Iye ndi Yemwe amandichiza. | وَإِذَا مَرِضْتُ فَهُوَ يَشْفِينِ. |
| Palibe wopembedzedwa wina kuposa Iye. | لَآ إِلٰهَ إِلَّا هُوَ. |
| Iye ndi Mwini wa zonse zili kumwamba ndi dziko lapansi. | لَهُ مَا فِي ٱلسَّمَاوَاتِ وَمَا فِي الْأَرْضِ. |
| Ndipo Iye ndiwakutha kuchita chilichonse. | وَهُوَ عَلَىٰ كُلِّ شَيْءٍ قَدِيرٌ. |

تَمْرِيْنٌ

**NTCHITO**

1. **Kodi Allāh ndi ndani?**

   Mufunseni mwana kuti Allāh ndi ndani ndipo afotokoze mosonyeza kuti wamudziwadi Allāh.

2. **Nanga adatilenga ndi ndani?**

   Mwana afotokoze yemwe adatilenga ife. Ana asakhulupirire kuti chilengedwe chinangobwera chokha basi popanda wochilenga. Komanso asakhulupirire kuti Yesu ndiye Mlengi.

3. **Kodi palinso wina amene ali wa mphamvu kuposa Allāh?**

   Mwana azindikire kuti Mwini Mphamvu zonse ndi Allāh. Azindikire kuti Allāh ndi Wakutha kuchita chilichonse chomuyenera Iyeyo mu Ulemerero Wake.

4. **Kodi amakuchiza ndi ndani ukadwala?**

   Mwana akuyenera kuphunzitsidwa akadali wachichepere nkhani yokhudza kudalira mwa Allāh. Mwana asakule ndi chikhulupiriro chodalira mwa anthu monga: asing'anga, abusa kapena ochita matalasimu.

5. **Nanga ndi ndani amene amatidyetsa tikamva njala?**

   Mwana azindikire kuti Mwini chisamaliro ndi Allāh. Palibe cholengedwa chimene chili pano pa dziko lapansi chomwe Allāh samachisamalira. Makolo sadyetsa mwana, koma iwowo ndi njira imene Allāh amadyetsera mwana.

# أَيْنَ اللّٰهُ؟

## ALLĀH ALI KUTI?

أَيْنَ اللّٰهُ؟

Kodi Allāh ali kuti?

اللّٰهُ فَوْقَ سَبْعِ سَمَاوَاتٍ.

Allāh ali pamwamba pa mitambo 7.

وَهُوَ عَلَى الْعَرْشِ كَمَا أَخْبَرَ[1]

بِلَا كَيْفٍ.

Ndipo Iye ali pamwamba pa ‘Arsh ngati momwe watiuzira posafunsa kuti ali pamenepo motani.

وَيَنْظُرُ إلى الْخَلَائِقِ.

Ndipo amaona chilengedwe Chake (zomwe chikuchita)

وَيَعْلَمُ مَا فِي ٱلْبَرِّ وَٱلْبَحْرِ.

Komanso amadziwa zomwe zili pa mtunda ndi m’nyanja.

وَمَا تَسْقُطُ مِنْ وَرَقَةٍ إِلَّا يَعْلَمُهَا.

Ndipo palibe tsamba lomwe limagwa kupatula kuti amalidziwa.

---

[1] Allāh sapezeka paliponse ngati momwe amayankhulira anthu ena. Iwo adasocheretsedwa ndipo akufuna kusocheretsa ena. Allāh ali pamwamba pa ‘Arsh yomwe ili pamwamba chilichonse.

تَمْرِيْنٌ

## NTCHITO

1. **Allāh ali kuti?**

   Mwana afotokoze komwe kuli Allāh. Ena mu gulu la asilamu amakhulupirira kuti Allāh amapezeka pali ponse. Izi sizolondola ndipo ndi chikhulupiriro cholakwika.

2. **Kodi Allāh alipo mungati?**

   Gawo ili ndi lofunikira chifukwa mwana amacheza ndi anzake amene sali asilamu ku sukulu zomwe akupita, kapena anzake amene mwayandikana nawo nyumba. Ena mwa ana amenewo akuphunzitsidwa ndi makolo awo kuti milungu ilipo itatu.

3. **Kodi pali chimene Allāh samachidziwa?**

   Mwana akuyenera kuphunzitsidwa kuti Allāh amadziwa chilichonse chimene adachilenga. Amadziwa mmene chilili komanso kumene chimakhala. Amadziwa zomwe chimachita mu mdima komanso mu usana. Ndipo palibe chomwe chili chobisika kwa Iye.

4. **Tinganene kuti chani pamene wina akutiuza kuti Allāh ali paliponse?**

   Apa kholo kapena mphunzitsi amuuze mwana zoyenera kunena pamene ena akumuuza kuti Allāh ali paliponse.

# مِنْ صِفَاتِ اللهِ

## ZINA MU MBIRI ZA ALLĀH

| | |
|---|---|
| Allāh samadya | اللهُ لاَ يَأْكُلُ. |
| Ndipo Iye salakwitsa | وَلاَ يَضِلُّ. |
| Komanso Iye samaiwala | وَلاَ يَنْسَى. |
| Sikumamupeza kuodzera ngakhalenso tulo. | لَا تَأْخُذُهُۥ سِنَةٌ وَّلَا نَوْمٌ. |
| Iye ndi Wamoyo ndipo samwalira. | وَهُوَ حَيٌّ لَا يَمُوتُ. |
| Iye ndi Amene amamva Pempho (limene kapolo Wake akumupempha) | أَنَّهُ يَسْمَعُ الدُّعَاءَ. |
| Komanso amamudziwa yemwe akugwira ntchito mwa Ikhlās ndi uyo amene akuchita pofuna kuti ena amuone. | وَيَعْلَمُ الْمُخْلِصَ والْمُرِيْءَ. |
| Ndipo Allāh amachita zomwe Iye wafuna. | وَيَفْعَلُ اللَّهُ مَا يَشَاءُ. |

| | |
|---|---|
| اللَّهُ يَضْحَكُ. | Allāh amaseka. |
| وَأَنَّهُ يَغْضَبُ. | Ndipo Iye amakwiya. |
| وَاللَّهُ سُبْحَانَهُ يَتَكَلَّمُ. | Komanso Allāh Woyeretsedwa amayankhula. |
| وَكَلَامَهُ لَيْسَ مَخْلُوقٌ. | Ndipo mawu Ake si chinthu cholengedwa. |
| وَمَا يَخْرُجُ مِنْهُ إِلَّا حَقٌّ. | Ndipo palibe chimene chimatuluka kuchokera kwa Iye kupatulapo chilungamo. |
| وَلِلَّهِ وَجْهٌ وَعَيْنَانِ. | Allāh ali ndi nkhope komanso maso awiri. |
| وَلَهُ يَدَانِ وَقَدَمٌ وَأَصَابِعَ.[2] | Iye ali ndi Manja awiri, Mwendo komanso Zala. |
| وَلَا تُمَثِّلُ صِفَاتِهِ بِصِفَاتِ خَلْقِهِ. | Ndipo musazifananize Mbiri Zake ndi mbiri za chilengedwe Chake. |
| لِأَنَّ اللَّهَ لَيْسَ كَمِثْلِهِ شَيْءٌ. | Chifukwa ndithudi Allāh sali wofanana ndi chilichonse. |
| فَكَذَلِك صِفَاته لَيْسَتْ فِي الدُّنْيَا. | Pa chifukwa ichi, Mbiri Zake sizili pa Dziko lapansi pano (safanana ndi zolengedwa Zake). |

[2] Swahīh Al-Bukhārī, #4919; Muslim, #183; Muslim, #2654; Muslim, #1827; Al-Bukhārī, #4684; Sūrah Swad 38:75; Sūrah Al-Qamar 54:14; Sūrah Ar-Rahman 55:27

# تَمْرِيْنٌ

## NTCHITO

1. **Kodi Allāh amafanana ndi munthu?**

   Mulongosolereni mwana kuti Allāh kukhala ndi zizindikiro zomwe zatchulidwa mu Qur'ān komanso Sunnah, sizikusonyeza kuti Iye amafanana ndi munthu kapena chimodzi mu zolengedwa Zake.

2. **Allāh ali ndi Manja angati?**

   Manja a Allāh onse awiri ndi akumanja (Right Hands). Izi zikufotokozedwa mu hadīth ya 'Abdullāh Ibn 'Umar yomwe adaisunga Muslim (#1827).

3. **Kodi Allāh ali ndi zala zingati?**

   Palibe chiwerengero cha zala za Allāh. Mtumiki wa Allāh ﷺ mu hadīth ya 'Abdullāh Ibn 'Amr Ibnil 'Āsw (*Muslim #2654*) sadatchulemo kuti Allāh ali ndi zala mwakuti. Ife tingokhulupirira kuti Allāh ali ndi zala ndipo tisalimbane ndi kumafunsa kuti zilipo zingati.

   Mitima yathu ili pakati pa zala ziwiri za Allāh kuchokera mu zala Zake, ndipo amaitembenuza momwe Iye wafunira. Pachifukwa ichi, muphunzitseni mwana kukhala womamupempha Allāh kuti asautembenuze mtima wake kuti ukanire Chipembedzo Cholondolachi.

4. **Kodi Allāh amaseka?**

   Mwana akuyenera kuphunzitsidwa kuti Mbuye wake amaseka. Pa chifukwa ichi, mwanayo sadzataya chiyembekezo mwa Allāh chifukwa adzazindikira kuti Allāh ndi Wachisoni kwambiri kwa akapolo Ake.

# الْإِيْمَانُ

**CHIKHULUPIRIRO**

| | |
|---|---|
| Kodi Chikhulupiriro ndi chiyani? | مَا الْإِيْمَانُ؟ |
| Kumeneku ndiko kukhulupirira mwa Allāh, | الإِيمَانُ: أَنْ تُؤْمِنَ بِاللّٰهِ، |
| Komanso mwa Angelo Ake, | وَمَلَائِكَتِهِ، |
| Ndi mwa Mabuku Ake, | وَكُتُبِهِ، |
| Ndi mwa Atumiki Ake, | وَرُسُلِهِ، |
| Ndi mwa Tsiku la Chiweruzo, | وَالْيَوْمِ الآخِرِ، |
| Ndi mwa Jannah komanso Moto, | وَالْجَنَّةِ وَالنَّارِ، |
| Ndi mwa Qadar – zabwino zake ndi zoipa zake | وَالْقَدَرِ خَيْرِهِ وَشَرِّهِ.[3] |

[3] Musnad Ahmad, #184; Musnad Al-Bazzār, #4832; Muslim, #8

# تَمْرِيْنٌ

**NTCHITO**

1. **Kodi Chikhulupiriro ndi chiyani?**

   Mwana alongosole nsanamira za chikhulupiriro chake. Kuchokera mu gawo ili, mwana adziwe kuti iyeyo sangakhale msilamu pokhapokha atakhulupirira mu nsichi zimenezi komanso kuzidziwa bwino lomwe.

2. **Kwa yemwe wakanira mwa Allāh zili bwanji pa iye?**

   Mwana adziwe kuti kukanira mwa Allāh ndi *kufr* ndipo kufr gwero lake ndi ku Moto basi. Kupatula uyo amene wachita mwa umbuli, mokakamizidwa komanso molakwitsidwa mu kamvetsetsedwe ka āyah kapena hadīth.

3. **Kodi ndi zoyenera kukhulupirira mwa atumiki onse?**

   Mwana aphunzitsidwe kuti atumiki onse a Allāh ndi oyenera kutsatiridwa. Pasakhale kusiyanitsa pakati pa mtumiki wina ndi wina. Onse uthenga wawo udali wofanana.

4. **Kodi anthu amene adamwalira kalekale adzadzutsidwanso?**

   Afotokozeredwe mwana kuti Tsiku la Chiweruzo, Allāh adzasonkhanitsa anthu a mibadwo yonse kuyambira pa bambo athu Adam mpaka kufikira pa munthu womaliza kubadwa pa dziko pano.

# مِنَ الْإِيمَانِ بِاللَّهِ

**KUCHOKERA MU KUKHULUPIRIRA MWA ALLĀH**

| | |
|---|---|
| الْإِيمَانُ بِمَا وَصَفَ بِهِ نَفْسَهُ فِي كِتَابِهِ | Chikhulupiriro mu mbiri zomwe Iye wadzifotokoza nazo Mwini Wake mu Qur'ān. |
| وَبِمَا وَصَفَهُ بِهِ رَسُولُهُ مُحَمَّدٌ ﷺ | Ndi mbiri Zake zomwe wazifotokoza Mtumiki Wake Muhammad ﷺ. |
| مِنْ غَيْرِ: تَحْرِيفٍ وَلَا تَعْطِيلٍ | Popanda kuzisintha (mbirizo) komanso kuzikana. |
| وَمِنْ غَيْرِ: تَكْيِيفٍ وَلَا تَمْثِيلٍ. | Komanso popanda kufunsa kuti mbirizo zili motani kapenso kuzifananizira (ndi zolengedwa Zake). |
| بَلْ نُؤْمِنُ بِأَنَّ اللَّهَ تَعَالَى: | Koma kuti timakhulupirire zoti ndithudi Allāh Wapamwambamwamba: |
| لَيْسَ كَمِثْلِهِ شَيْءٌ. | Sali wofanana ndi chilichonse. |
| فَلَا نَنْفِي عَمَّا وَصَفَ بِهِ نَفْسَهُ. | Ndipo sitizikana mbiri zimene wazifotokoza nazo Mwini Wakeyo. |
| وَلَا نُحَرِّفُ: الْكَلِمَ عَنْ مَوَاضِعِهِ. | Komanso sitiwasuntha Mawuwo pa malo ake (powasintha matanthauzo ake enieni). |

تَمْرِيْنٌ

**NTCHITO**

1. **Kodi zili zolondola kusintha tanthauzo la Mbiri za Allāh?**

   Mwana aphunzire kuti Mbiri za Allāh sizikuyenera kufotokozedwa malinga ndi momwe ife timafunira. Koma kuti zifotokozedwe malinga ndi momwe Allāh ndi Mtumiki Wake (ﷺ) adafotokozera. Ndipo pasakhale kusintha kulikonse mu kafotokozedweko.

2. **Zili bwanji pa yemwe wakanira mu Mbiri za Allāh?**

   Mwana adziwe kuti kukanira mu Mbiri za Allāh ndi *kufr* ndipo kufr gwero lake ndi chilango cha Moto. Kupatula uyo amene wachita mwa umbuli, mokakamizidwa komanso molakwitsidwa mu kamvetsetsedwe ka āyah kapena hadīth.

3. **Kodi ndi zoyenera kukana kuti Allāh ali ndi Maso?**

   Mwana akuyenera kuunikiridwa momveka bwino kuti mbiri za Allāh sizikuyenera kukanidwa. Zikhulupiriridwe m'mene zililimo.

4. **Nanga kunena kuti Allāh amatopa ndi zoyenera?**

   Mwana adziwe kuti Mbuye wake satopa ndipo sapumula. Iye ali tcheru nthawi zonse ndipo palibe chimene chimamuphonya.

5. **Kodi tingamunene Yesu kuti ndi Mulungu?**

   Afotokozeredwe mwana mbiri za Allāh ndi mbiri za munthu. Chifukwa mbiri ziwirizi ndi zosiyana kwambiri.

# الشَّيْطَانُ

**SATANA**

| | |
|---|---|
| Kodi Satana ndi ndani? | مَنْ هُوَ الشَّيْطَانُ؟ |
| Iye ndi Iblīs ndipo ndi cholengedwa cha Allāh. | هُوَ إِبْلِيْسُ وَهو مِنْ خَلْقِ اللَّه. |
| Ndithudi iyeyu ndi woyambirira mwa omunyozera Allāh | وإِنَّهُ أَوَّلَ مَنْ عصَى اللَّه. |
| Komanso iye ndi mtsogoleri wa ma satana onse. | وَهُوَ رَأْسُ الشَّيَاطِين. |
| Mu gulu la ma satana, palibe amene ali wokhulupirira. | وَأَمَّا الشَّيَاطِيْنُ فَلَيْسَ فِيْهِمْ مُؤْمِنٌ. |
| Iblīs ndi mdani wa Allāh komanso mdani wa okhulupirira. | وإِبْلِيْسُ عَدُوٌّ اللَّهِ وَعَدُوٌّ الْمُؤْمِنِيْنَ. |
| Iyetu ndi amene amalowa mu mitima ya anthu. | وَهُوَ الَّذِيْ يَدْخُلُ فِي صُدُورِ النَّاسِ. |
| Kenako amaikamo chikaiko m'mitima yawoyo. | فَيُوَسْوِسُ فِي صُدُورِهِمْ. |
| Pamene iwo amukumbukira Allāh, iye amadzibwenza ndipo amatulukamo (m'mitimamo). | فَإِذَا ذُكِرَ اللَّهُ خَنَسَ وَخرَجَ. |

تَمْرِيْنٌ

**NTCHITO**

1. **Kodi Satana ndi ndani?**

   Mwana azindikire kuti pamene wabadwa, iye ali pa nkhondo yaikulu kwambiri yogonjetsa Shaytwān.

2. **Amene adalenga Satana ndi ndani?**

   Mwana adziwe kuti Shaytwān ndi cholengedwa cha Allāh. Ndipo Shaytwān alibe mphamvu yoyendetsa dziko lino.

3. **Kodi ma Satana amakhulupirira mwa Allāh?**

   Mwana akuyenera kuunikiridwa kuti palibe chiwanda choipa chimene chili chokhulupirira mwa Allāh.

4. **Kodi ma Satana bambo wawo ndi ndani?**

5. **Kodi mdani wathu ndi uti?**